

Danieli : 8:1-13

Mutu : Masomphenya a nkhosa ndi tonde

Landirani moni wa Kumwamba inu wokondedwa anzanga apaulendo. Lero tiyeni titsogozedwe ndi mau a Mulungu apa Marko 16:16, pamene Ambuye Yesu akuti, “Amene akhulupirira nabatizidwa, adzapulumutsidwa; koma amene sakhulupirira adzalangidwa.”

Tsono mupologalamu yatha, tinali kusanthula Danieli 7:14-28, momwe tinakambirana za kumasulira kwachirombochachinayi. Ndipo lero pa Danieli 8:1-13, tiunika za masomphenya a nkhosa ndi tonde.

Danieli 8

Pano ndifuna ndiyambe ndi mau akuti, masomphenya amene analembedwa ndi Danieli m’chapter chino anali ulosi,panthawi yomwe anaperekedwa kwa iye, koma pano masomphenyawo akwanitsidwamooneka bwino.

Tere, ichi ndi chapter chomwe muli nkhani ya masomphenya a mneneri Danieli m'chaka cha chitatu muulamuliro wa mfumu Belisazara. Danieli nthawi imene anali mumzindawa Susa, m'chigawo cha Elamu. Ndiye alikumeneko, m'amasomphenya anaona nkhoa yanyanga ziwiri, nyanga ina yokwera pamene ina inali yotsika. Ndinyangazimenezi nkhoa ija inali kugunda zinthu ndi mwamphamvu zake, kumadzulo ndi kumpoto ndi kum'mwera kotero kuti panalibenso chinthu china chomwe chikanakhozakuletsa kapena kulimbapakukhomako.

Ndiye pamene anali chiyang'anire, anaona tonde (mbuzi ya mphongo), ikuchokera kumadzulo ikudumpha m'mwamba kenakandikugwa pansi ndi nyanga yake imodzi yomwe inali pakati pamaso pake. Taonani tonde uyu, anagunda nkhoa ija kotero kuti nyanga zake zinathyokakotheratu. Tsono tondeyu anaonetsa mphamvu zake zonse, koma patapita nthawi, nyanga ija inathyoka ndipo pamalo pake, panameranyanga zina zinayi. Kuchoka panyangaimodziyi, panaturukakanyangakakang'onokamenekanakhalakamphamvu ndi

kofunika, kamenekanaloza kum'mwera ndi kum'mawa, ku dziko lokongola la Palestine.

Nyanga imeneyi, inaonetsa kuti inali yamphamvu kotero kuti inali kumenyana ndi zam'mwamba monga nyenyezi ndipo inazigwetsa pansi. Tsono nyanga imeneyi inadziwonetsa yokha kukhala yamphamvu kwamkulu wa zam'mwamba, ndipo analetsa nsembe zonse za m'kachisi pambuyo pake ndi kumugwetsamkuluyu pansi. Ndiye pamene woyera mtima anali kakasinafunsana kuti kodi zimenezi zidzachitika mpaka liti? Ndipo yankho linati zidzakhala zikuchitika kwa masiku zikwi ziwiri ndi mazana atatu kufikira pamene Kachisi adzayeretsedwanso.

Ndiye zitatha izi, tikumva kuti mngelo Gabrieli anatumidwakukamasulira masomphenyawo kwa mneneri Danieli. Apa ndipo pamene analengeza kuti nkhusa ya nyanga ziwiri ija, ikuimira mafumu ya Amedi ndi Peresiya; pamene tonde uja anali kuimira mfumu ya a Greek. Tsono nyangayaikuru pakati pa maso ake ndiyo mfumu yoyamba pamene nyanga zinayi zija zimene zinathyoka zikuimira kugawikapanayikwa ufumuwu. Tsono nyangayaing'ono ndiyo mfumu yoomsam'maonekedwe ake imene

ndiyoukira mfumu ya mafumu, yomwe pambuyo pake idzaonongekakotheratu. Ndiye kumasulira kwa mau awa, ndiko kumene kunasautsa Danieli kwanthawiyaitali.

1. Chaka chachitatu cha Belisazara mfumu masomphenya anandionekerakwa ine Danieli, atathakundionekeraoyamba aja.

Danieli akulemba kuti masomphenya awa, anaonetsedwa m'chaka chachitatu cha ulamuliro wa Belisazara, amene anali mfumu yotsiriza ya Babulo. Mukumbukira kuti masomphenya amene Danieli anaona m'chapter 7, ndiwo amene anaperekedwa m'chaka choyamba cha ulamuliro wake. Tsono masomphenya onsewa anaoneka kumapeto kwa ulamuliro wa Babulo.

2. Ndipo ndinaona m'masomphenya; tsono kunali pakuwaona ine ndinalim'Sunsani, m'nyumba ya mfumu ndiwo m'dziko la Elamu; ndinaona m'masomphenya kuti ndinalikumtsinjeUlayi.

Tsono Danieli anali kuona masomphenya awa pamene anali ku Sunsani, amene amatchedwanso Susa, likulu la ufumu wa Amedi

ndi a Peresiya. Koma akutsindika kutimasomphenyawaanaonekera kwa iye, ndipo anali kulingalira kwambiri ndi cholinga chakuti amvetsetse.

Pano ndikoyenera kunena kuti masomphenya awa anaonekakwa Danieli pamene anali ku Sunsani, m'nyumba yachifumu ya a Peresiya, yomwe inali m'mbali mwa mtsinje wa Ulayi. Tsono chigawo cha Elamu chomwe ndi cha Peresiya, chinali kufupi ndi Babulo. Ndiye tikunena kuti Danieli sanapiteko ku Sunsanimtupi ayi, popeza anali ku Babulo ngati kapolo, kotero kuti sikukanakhalakotheka kupita kunyumba yachifumu ya m'dani wa Babulo. Tere tikunenetsa kuti Danieli anali ku Sunsanimumzimu monga muja mneneri Ezeieli anali kupezeka ku dziko la Israeli mumzimu pamene mtupi, anali ku Babulo. Ndiye tikunena kuti masomphenya awa, anali kukhudza ufumu wachitatuwa Amedi ndi Peresiya, kotero kuti anapatsidwa chithunzi choonetsakuti anali kumeneko.

Wokondedwa anzanga apaulendo, nkhani iyi ikunena kuti Mzimu wa munthu ukhoza kukhala womasulidwa ngakhale mwini wakeyoatakhala kuti ndiwomangidwa. Kutsindika kunena kuti

pamene ife tikhala womangidwa, Mzimu wa Mulungu sumangidwa ayi.

3. Ndipo ndinakweza maso anga ndi kupenya; taonani panaimapamtsinje nkhusa yamphongoyokhala nazo nyanga ziwiri, ndi nyangaziwirizo zinali za msinkhuwautali, koma imodzi inaposainzake; yoposayoinaphuka m'mbuyo.

Pano tiyeni tigwire mau akuti, “Koma imodzi inaposainzake; yoposayoinaphuka m'mbuyo.” Nkhani ikunena kuti nyangaziwirizi zikuimira ufumu wa Amedi ndi Peresiya. Ndiye nyanga yomwe ikuimira Amedi ndiyo imene inaphuka poyamba, kunena nthawi yomwe Gobrusi, mkuluwa nkondo wa Amedi, anaononga mzinda wa Babulo. Koma pambuyo pake ndipo pamene ufumu wa Peresiya unaphuka ndipo kuti unakula kwakukuru. Kutanthauza kuti nkhusa yamphongo iyi, yokhala ndi nyanga ziwiri, momwe nyanga imodzi ndi yaitari kuposa inzake, zikuimira ufumu wa Amedi ndi Peresiya momwe a Peresiya anatenga mphamvu zochuluka. Tere pano tikutha kuona mau aja amati woyamba ndiwo adzakhala wotsiriza ndi wotsiriza adzakhala woyamba. Monga adanena Ambuye Yesu pa Mateyu 19:30, pamene akuti, “Koma ambiri

oyamba adzakhala akuthungo, ndi akuthungoadzakhala oyamba.” Izi, ndizomwe zinachitika ndi ufumu wa Peresiya, umene unaphuka pambuyo, ndiwo unakhala woyamba.

4. Ndinaona nkhusa yamphongoirikugunda kumadzulo ndi kumpoto ndi kumwela ndi ndipo panalibe zamoyo zikhoza kuima pamaso pake; panalibensowakulanditsa m’dzanja lake koma inachita monga mwa chifuniro chake, nidzikulitsa.

Ndime ino, ikufotokonza nkhanu ya kukulakwa ufumu wa a Peresiya. Taonani pamene nkhusa yamphongoyiikugunda kumadzulo, ndiye kuti akunena za kuthira nkundo pa maiko a Syria, Greece ndi Asia. Pamene kumpoto akunena za kuonongeka kwa mitundu ya Lydia, Armeniya ndi A Scythia ndipo kum’mwera akukamba za kuthyola mitundu ya Arabiya, Ethiopia ndi Agupto. Awa, ndiwo maiko amene anapanga ufumu wa Peresiya. Kutanthauza kuti Peresiya anakhala ufumu wamphamvu, kotero sipanapezekensonyangaikanaima naye. Ufumu wa Peresiya unali waukulu chifukwa unali ndi mphamvu zochuluka mkati ndi kunja komwe. Apa, ndipo Peresiya anafika ponena kuti Waukulu konsekondi iye, popeza kunalibe wina aliyense womposa, kotero

kuti anali kuchita chomwe angafune. Kunena kuti ufumu uwu, ndiwo unali kukulambali zonse ndipo ndi ufumu uja unali kuimira chimbalangondo m'chapter 7. Tsono tiyenera kunena kuti ngakhale ufumu unali kukula chomwechi, koma sanali kudziwa kuti kuchita chinthu chabwino, ndiko kumapanga munthu kukhala wamphamvu.

5. Ndipo polingirirapo ine, taonani wadza tonde wochokera kumadzulo, pa nkhope ya dziko lonse lapansi, wosakhudza nthaka; ndi mbuziyo inali ndi nyangayooneka bwino pakati pa maso ake.

Tsono taonani kuti pamene Danieli anali kulingalira za mphamvu ndi luso la nkhusa ya mphongo ija, koma taonani kuti kutari kumadzulo kunaturukira tondewanyanga imodzi yamphamvu. Ndiye tondeuyu, akuimira ufumu wa a Greek, momwe Alexander anali mfumu yawo yaikulu. Tsono nkhanu ikuti pamene mfumu Xerxes mfumu ya Peresiya imayesakukulitsa ufumuchakumadzulo, koma kuchokera kumadzuloko, kunaturukatonde amene analikudza mofulumira. Uyu ndiye Alexander ndi gulu la asirikari ake, amene anadza ndi mphamvu zake zonse kuthyola maiko onse

apansi pano, kotero kuti atatha, anakhala pansi ndi kulira popeza panalibenso dziko lomwe akanathyola. Uyu, ndiye uja pa Miyambo 30:31, akumutchula kuti, “Kavalo wolimba m’chuuno ndi tonde, ndi mfumu yokhala ndi ankhondo ake.” Kutsimikiza kuti Alexander, ndiye mfumu amene anali ndi mphamvu zodzimva, kotero kuti kunalibe ufumu ndi umodzi womwe umene ukanaima ndi iye. Momwemo lero lino aliponso anthu ena amene amadzimva kuti ndiwo wopambana ena onse ngakhale pochita uchimo. Koma tamvani mau a Mulungu pa Miyambo 3:34, akunena kuti, “Anyozadiakunyoza, koma apatsaakufatsa chisomo.” Kutanthauza kuti inu muyenera kudzichepetsa kuti mukhoze kulandira chisomo cha Mulungu. Mwanjira ina tikunena kuti palibe munthu amene amalandira chisomo pamene akudzimva kukhala wopambana ena onse.

6. Ndipo anadzera nkhosa yamphongoyoyokhala ndi nyanga ziwiri imene ndidaionairikuimakumtsinje, naithamangira ndi mphamvu yake yaukali.

7. Ndipo ndinamuona wayandikira pafupi pa nkhosa yamphongo, nawawidwa mtima nayo, naigunda

nkhosayamphongo, nathyolanyanga zake ziwiri, ndipo mphongoyoinalibe mphamvu yakuima pamaso pake, koma anaigwetsa pansi, naipondereza; ndipo panalibe wakupulumutsamphongoyom'dzanja lake.

Tsono Ulayi ndiwo malo pamene panachitikira nkhondo ya Peresiya ndiGreece.Ndiye nkhanu ikuti, pamene Danieli anali kulingalirabe za zomwe inachita nkhosa yamphongo ija, anaona tondeakuturuka kumadzulo kufika padziko lonse ndi ukali ndi kuponda nkhosa yamphongo ija ndi kuigwetsa pansi. Tsono pamene tiwerenga Danieli 8:21, tipeza kuti tonde uja malinga ndi kumasulira kwa mngelo, akuimira Alexander mfumu ya Greece ndi Makedoniya, amene akudza kudziko ndi mphamvu. Tere pano wathyola ufumu wa Amedi ndi Peresiya, kunena kuti tondewathyolanyanga ziwiri za nkhosa yamphongo. Kutanthauza kuti Dariyo alibenso mphamvu yakuti akhoza kuima ndi Alexander ayi komanso alibe abwenzi amene akhoza kumuthandizakumulanditsa m'dzanja la mdaniyo.

Wokondedwa anzanga apaulendo ndifuna muone kuti maufumu onse amene anali ndi mphamvu, sanagwiritse bwino mphamvu zawo chifukwa panalibe amene akanawatsutsa, kotero kuti

sanadziletse kuchita choipa chilichonse. Leronso alipo atsogoleri ambiri amene chifukwa cha mphamvu, sadziletsa kuchita choipa ayi. Kodi inu paudindo wanu mumamva kudzudzula kwa anthu ena?

8. Ndipo tondeyoanadzikulitsa kwakukuru, koma atakhala wamphamvu, nyanga yake yaikuruinathyoka; ndi m'malo mwake munaphukanyanga zinayi zooneka bwino, zoloza ku mphepo zinayi za mlengalenga.

Mundime ino ndifuna tigwire mau akuti, “Koma atakhala wamphamvu, nyanga yake yaikuruinathyoka.” Tsono mwina mwafunsa kale kuti, kodi ndichiyani chomwe chinathyolanyangayo? Yankho likuti, panalibe yemwe akanathakuthyolanyanga ya tondeyi. Kutsimikiza kuti pamene Alexander anakhala mfumu ya Greece, dziko lonse lapansi linali pansi pa ulamuliro wake. Apa, ndipo pakubwera mau aja akuti, “Pamene Alexander, The Great, atamaliza kuthyola maiko onse padziko lapansi, kenaka anakhala pansi ndi kulira, popeza panalibenso dziko lina lomwe sanalithyole.” Koma taonani kuti pamene anali kudzimva motere, tiona kuti tsiku lina analedzera

usiku wonse ndipo anafa usiku womwewo m'chaka cha 323 B.C, pamene anali ndi zaka 32. Tikunena kuti pamene Alexander, The Great, anali ndi mphamvu, ndipo pamene nyangainathyoka. Kutsindika kuti ufumu wonse waukulu wa Alexander the Great, unathyoka chifukwa cha mowa. Tikunena kuti Alexander anali ndi mphamvu zochuluka, kotero kuti panalibe ufumu wina ukanakhozakuthyola ufumu wake. Koma mwachisoni kuti ngakhale Alexander anathyola maufumu onse, koma analepherakuthyola mtima wake. Kutanthauza kuti Alexandera analibe mtima wodziletsa. Tsono nkhani ikunena kuti anthu ambiri ambiri lero lino alibe mtima wodziletsa, koma sakudziwa kuti akupita ku chionongeko. Tere ine ndikuti Uthenga uwu, ukupitakwa inu kukuchenjezani kuti muli kupita kuphompho.

9. Ndipo mu imodzi ya izi munaphukanyangayaing'ono, imene inakhala kwakukuru ndithu kuloza kumwela ndi kum'mawa ndi ku dziko lokometsetsa.

Tsono tisanapite patari ndifuna kudziwitsa kuti “dziko lokometsetsa” likunena za dziko la Israyeli. Ndiye nyangayaing'ono m'chapter chino ikusiyana ndi nyangayaing'ono m'chapter 7. Mu

chapter chimenechi, tidapeza kuti
nyangayaing'onoinaturukamuufumuwachinayi. Ndipo
nyangayaing'ono m'chapter chino, ikuturukamuufumuwachitatu.
Uwu, ndiufumu womwe ukuturuka mu ufumu wa Syria, momwe
mfumu yake ndi AntiokasiEpifane, amene anatchuka lakuti,
“Munthu wamisala.”

Tsono Antiokasi ndiye anakhala pampando wakulamula m'chaka
cha 175 B.C. pamene anakaputa mzinda wa Yerusalemu. Tere
ndichifukwa cha iyeyu kuti amakabiniautsidwe ndi cholinga
chofuna kuletsa ulamuliro waAntiokasi. Uyu, ndimunthu amene
anayesapo kuononga a Yuda onse, koma sanakwanitse. Tere,
anangoikachifano cha Jupiter m'malo oyera m'kachisiwa Mulungu
mu Yerusalemu. Ichi, ndicho chinali chonyasachoiikika m'malo
oyera. Koma pambuyo pake anathirazipwidza za
nkhumbapazipangizo zonse zoyera za m'kachisiwa Mulungu.

Wokondedwa anzanga apaulendo, nkhani ikunena kuti
AntiokasiEpifane, anali kukangana ndi ana a Mulungu,
amenealiaufumu wa Kumwamba. Kutsindika kuti Antiokasi anali
kunyazitsa mphamvu ndi ulamuliro wa Mulungu wa a Yuda. Ndiye

tikunenetsa kuti munthu aliyense amene azunza ana a Mulungu, ndiye kuti akukanga ndi Mulungu mwini. Ndikunena mau amenewa chifukwa Antiokasi anafika pomatenga nsembe zomwe Mulungu analamula kuti ziziperekedwa m'mawa uliwonse paguwalansem'kachisi. Apa, tikunenetsa kuti Antiokasiana onongadi Kachisi wa Mulungu ngakhale sanagumule, koma ana onongapaikamo ndi kuchitamozonyasa. Kodi lero sizilikuchitika m'ma church athuwa? Kapena tifunse kuti, kodi inu simukuononga Kachisi mwakuikamo chodetsa?

12. Ndipo khamulo linaperekedwa kwaiyo, pamodzi ndi nsembe yopserezayachikhalire mwa kulakwa kwake, nigwetsa pansi choonadi, nichita chifuniro chake, nikuzika.

13. Pamenepo ndinamva wina woyera akukunena; ndi wina woyera anati kwa iye uja wanenayo, masomphenya a nsembe yopserezayachikhalire ndi cholakwachakupululutsa cha kupereka malo opatulika ndi khamulo ziponderezedwe, adzakhala mpaka liti?

Tsono munkhani yonse ndifuna tione kuti Antiokasianaimika fano lake ndi cholinga chofuna kupondereza choonadi cha Mulungu,

chimene chinali m'buku la chilamulo.Kutanthauza kuti Antiokasindiye anapyola muyeso pakuchitira Mulungu mwano.Koma samayenera kusangalalakotheratundikuyesa kuti wapambana Mulungu ayi.Tikunenetsa kuti m'dani wa a Yuda uyu, sakanakwanitsakuchitsa zonse pakakhala kuti Mulungu sanalore zimenezi. Kutanthauza kuti Mulungu ndiye anaika mphamvu yake m'dzanja la Antiokasi.

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndifuna inu ndi ine tione kuti muli dzanja la Mulungu muntchito zonse za adani a mpingo. Kutsimikiza kuti adani a mpingo ndiwo amakhala mkwapulowa ana a Mulungu m'dzanja la Mulunguyo. Kutanthauza kuti Mulungu sakanalola adani a mpingo kutenga mphamvu pakanakhala kuti ana ake sadamutokosemwakuchita uchimo. Tere, apa tikunenetsa kuti Antiokasi anali kugwiritsidwa ndi Mulungu pakulanga Israeli chifukwa cha nsembe zosayenera.

Anzanga ndifuna titsirize ndi mau akuti, kupambana kwa m'dierekezi ndi kwanthawiyochepa chifukwa Mulungu akuwerenga nthawi yake ndipo ikakwana, woipa amayesa tsoka. Kutsindika

kuti inu ndi ine, tiyenera kudziwa chifuniro cha Mulungu kudzera mwa mwana wake Yesu Kristu.

Lero tilekeza pano. Koma timasanthulaDanieli 8:1-13, momwe timaunika za masomphenya a nkhosa ndi tonde.

Ambuye akudalitseni inu lero. Amen!